

Kodi ico ndi ciani?



Mau ofanana ndi mau obvuta opezeka **m'Baibulo**
la m'Chichewa

Kodi ico ndi ciani?

Baibulo lomwe limagwiritsidwa nchito ku Petauke ndi lolembedwa m'Chichewa. Muli mau osadziwika ndi iwo olankhula Cinsenga kapena Cinyanja.

M'bukuli mupeza mau ofanana ndi mauwo osadziwika.

Mawuwa ali motsatira zilembo za alfabeti.

Malangizo ogwiritsira nchito bukuli

1. Werengani Baibulo tsiku ndi tsiku. Mukakomana ndi liu losadziwika, tengani bukuli.
2. Yang'anirani cilembo coyamba ca liu lomwe mufuna kudziwa liu lofanana nalo.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula*, cilembo ico ciyamba ndi *a*.
3. Pitani patsamba lomwe cilemboci calembedwa ndi cilembo cacikulu.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula* muyenera kupita pa tsamba lomwe A yalembedwa ndi cilembo cacikulu (tsamba 2).
4. Yang'anani cilembo caciwiri ca liu lomwe mufuna kudziwa liu lofanana nalo. Kenaka pitani pansi pamndandanda mpaka mutafika pa mau okhala ndi cilembo coyamba ndi caciwiri comwe mufuna.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula* mupite pansi pamndandanda mpaka mutafika pa mau oyambira ndi *a-n*.
5. Citani cimodzimodzi ndi cilembo cacitatu, cacinai ndi zina za liu lanu mpaka mutapeza liu lomwe mufuna kudziwa.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula*, londolani mndandanda a-n-a-n-g-u-l-a ndipo mudzaona kuti liuli ndi lopezeka pa tsamba 4.
6. Ngati liu limene mwapeza afunika cithunzi-thunzi, pezani cithunzi-thunzi ico pothera pa mau.
Mwacitsanzo, pansi pa liu lokamba kuti *anangula* ndi lolembedwa *onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a*. Mudzapeza cithunzi-thunzi ca *anangula* pa tsamba 6.



A



abibu	mwezi wa Ayuda uli pakati pa March mpaka pakati pa April
abira	nkhusa zazimuna
abuke	alemekezeke, afalitsidwe
abukitse	afalitse
acibakuwa	nsalu ya mtengo wapatali ya mtundu wa pepo
acifukize	apereke nsembe conunkhira bwino
acitando	akulu m'ufupi mwace
acizirezire	malo mwamene mumakhala mdima nthawi zambiri
adafocita	monga anacita nthawi zonse
adafokiza	nthawi zonse anapereka nsembe zonunkhira bwino
adafoika	nthawi zonse anaikapo zipangizozo
adafokhala	anali naye nthawi zonse
adafokwaniritsa	nthawi zonse anakwaniritsa masikuwo
adafomangidwa	kawiri-kawiri anali kumangidwa
adafopita	anapita
adafotero	anatero nthawi zonse
adafotsamira	anadalira pa munthuyo nthawi zonse
adafotsikira	anatsikira
adafowapambukirako	nthawi zonse anapambukirako
adafoyendayenda	anayendayenda kawiri-kawiri
adafukiza	adapereka nsembe zonunkhira bwino
adafunyulula	adabvungulula buku limene liri lopeteka, adatsegula buku
adalibukitsa	adalifalitsidwa, adalipatsidwa
adara	mwezi wa Ayuda uli pakati pa February mpaka pakati pa March
adatsotsa	adakhaliro kwa kanthawi, kukhala pa malo
adawinda	adalumbira
adayaruka	acita misala, asokonezeka
adazifunkha	adaziba, adaziwa mwankhanza kapena moopseza, adaziononga
adzabuka	adzapezeka, adzaoneka
adzabukitsa	adzafalitsa
adzabvimvinika	adzaomba manja, adzakondwera
adzadzombolera	adzathenulira
adzadzuma	adzabuula, adzphoalira kwambiri
adzafunkha	adzaba, adzaiwa mwankhanza kapena moopseza, adzaononga
adzajidimuka	adzalumpha
adzakufunkha	adzakubera, adzakuiwira mwankhanza kapena moopseza, adzakuononga
adzalamba	adzakakamizidwa kutumikira kapena kugwira nchito monga akapolo
adzalubza	adzasiya kumvera coonadi
adzandibukitsira	adzakulitsa mabvuto anga
adzandikumika	adzakhala pafupi ndi ine, adzakomana ndi ine
adzasula	adzaphwanya ndi kupanga cinthu cina
adzatsonya	adzaonetsa kuti cocitikaco ndi coipa, adzazizwa, adzadabwa
adzatsonyera	adzaonetsa kuti cocitikaco ndi coipa, adzazizwa
adzaubukitsa	adzaufotokozera, adzaufalitsa
adzawalaka	adzawapambana, adzawagonjetsa
adzawamezanitsanso	adzawalumikizanso
adzaweyeseka	adzanjenjemera
adzazifunkha	adzaziba, adzaiwa mwankhanza kapena moopseza, adzaziononga
adzifunkhira	anaiwa mwankhanza kuti akhale nazo zakuba
afukize	apereke nsembe zonunkhira bwino
afunkha	akuba, aiwa mwankhanza kapena moopseza, aononga

afunkhe	aiwe mwankhanza, akuba
afunkhidwa	aberedwa mwankhanza, aonongedwa, atengedwa mwankhanza
afunkhidwe	aberedwe mwankhanza
afunyulula	apanga mtambo kubweranso
afunyulule	akulitse
afunyululire	angelo aturutse mapiko ao
akaceteka	akasoceretsedwa
akadawazokota	akadawalemba pa mwala mwa kusewenzetsa kusema
akakombo	mtundu wina wa maluwa onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
akakulaka	akakupambana, akakugonjetsa
akamwiniatsatana	gulu lina la nyenyezi
akandilaka	akandipambana, akandigonjetsa
akapa	zisoti zansalu
akatumbu	nyama zina zimene zikhala m'madzi zimadya nsomba
akatungurume	mtundu wina wa cipatso monga kashonati onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
akerubi	mtundu wina wa angelo
akubukitsa	akufalitsa
akuceteni	akusoceretseni
akufukiza	munthu amene apereka nsembe zonunkhira
akufunkha	akuba, anthu oiwa mwankhanza kapena moopseza, anthu oononga
akufunyulula	angelo aturutsa mapiko ao
akukha	atulutsa
akulalira	acita udani, abisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
akundiwarukirawo	akundiseka, akundilankhulira monyozo
akunga	alingana, ali monga
akungudza	asiya malo kupeza malo ena, athawira
akupinduka	anthu amitundu amene adatembenukira kwa cipembezo ca Ciyuda (ca Aisrayeli)
akuseama	akhala pansi mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
akuwafunkha	akuwaba, akuwaiwa mwankhanza kapena moopseza, akuwaononga
akuwawawanya	akawalala, anthu oonongera
alakika	apambana, agonjetsa
alakike	apambane, agonjetse
alalira	acita udani, abisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
alauli	anthu a Mulungu amene anena za m'tsogolo
aleluya	lemekezani Yehova
alikufuliza	alikupeereka nsembe zonunkhira bwino
alikujiidimuka	ali kulumpha
alikulalira	acita udani, abisala ndi colinga kukacita coipa
alikuseama	ali kukhala pansi mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
alikuumatira	ali kufungatira
alipululutsa	aliononga kotheratu
alosa	aulula zinthu zimene zifunika kukacitika m'tsogolo
alosi	anthu amene alankhula zinthu za m'tsogolo
amafukizira	amapereka nsembe zonunkhira bwino
amaliwongo	anthu otsutsana naye
amangawa	angongole
amangofunkha	amangokuba, amangoiwa mwankhanza kapena moopseza, amangoononga
amarinyero	anthu oyendetsa bwato
ambanda	zigawenga, oononga, akupha, acifwamba
amcirakuyenda	oyendayenda opanda mtendere
amfunkhira	ambera mwankhanza
amikungudza	amitengo ya mtundu wina imene ili yaikulu ndi yolimba komanso imene imakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.

amipyololo	a makhala osiyana-siyana (yamizere-mizere)
amkungudza	a mtengo wa mtundu wina umene uli waukulu ndi wolimba komanso womwe umakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
amkuwa	a mwala wa kopa
amlalira	amcitira udani, abisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
amlombwa	a mtundu wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
am'nsinga	andende, akapolo
amphumphu	anthunthu, opanda cocotsapo, opanda cocokapo
amphwamphwa	olingana mu ufupi mwake ndi mu utali mwake
amsanje	malo yokwezedwa, malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
amtomera	amkatira
anabzong'onyoka	anapuluputa anagwa pansi nafa
anacilaka	anacipambana, anacigonjetsa
anaciwinda	anacilumbira
anadololoka	anabvutika kwambiri kotero kuti alibe ciyembekezo
anadzifula	anadziletsa okha kulowa m'ukwati ndi kukhala ndi mwana
anadzifunkhira	anaiwa mwankhanza kuti akhale nazo zakuba
anadziguguda	anadzimenya pacifuwa ndi dzanja
anadzindandalitsira	anadzikonzekera kucita nkondo, anadzikonzekera kutsutsa ndi Mulungu
anadzinika	asirikali adziika kuti akhale okonzeka kucita nkondo
anadzuma	anabuula, analira kwambiri
anafukizira	anapereka nsembe zonunkhira bwino
anafunkha	anaba, anaiwa mwankhanza kapena moopseza, anaononga
anafunyulula	anatsegula buku, angelo anaturutsa mapiko ao
anafunyululika	angelo anaturutsa mapiko ao
anagugitsa	anafoketsa, anaononga, anaipitsa
anaifukizira	anapereka nsembe zonunkhira bwino
anaiweyula	ananyamula nsembeyi m'manja mwake ndi kuiyendetsa uku ndi uku kuionetsa pamaso a Yehova
anakamulira	alamulira
anakanda	anaponda, anakanya
anakasuma	anacita ganyu kupeza ndalama, anasewenza kuti apeze cakudya
anakonkha	anasambitsa
anakumika	anakhala pafupi
analakika	anapambana
analikukunkhulira	anali kukunkhuluka
analikuseama	anali kukhala pansi mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
anamlaka	anampambana, anamgonjetsa
anamlalira	anamcitira udani, anabisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
anamlendewera	anamtsata momvetsera bwino kwambiri
anandandalika	anakhala m'magulu-magulu ankondo
anandandalitsa	anakhalitsa m'magulu-magulu ankondo
anangula	zitsulo zolembera zoletsa kusuntha kapena kuyenda kwa bwato onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
anangwape	nkhwangwa, khatema
anapiye	tiana ta nkuku
anapota	analuka, anasoka
anapsetsa mtima	anakwiyitsa
anapululutsa	anaononga kotheratu
anaseama	anakhala pansi mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
anasula	anapanga cinthu kucokera ku cinthu cina
anatilaka	anatipambana, anaticonjetsa
anatsalima	anapindamuka, anaponya kwendo kumbuyo
anatsimphina	anayenda cociriwa


anatsotsa	anapuma kwa kanthawi, anakhalira kwa kanthawi, kukhala pa malo
anaufula	anautenga
anawabuka	anapezeka, anadwala
anawafukizira	anawaperekera nsembe zonunkhira bwino
anawafula	anawaletsa kulowa m'ukwati ndi kukhala ndi mwana mwa kuwacitira cinthu cina kuti asabale
anawafunkha	anawabera, anawaiwira mwankhanza kapena moopseza, anawaononga
anawafunkhira	anawabera mwankhanza
anawakuzitsa	anawaoneketsa kuti ali apamwamba, anawakulitsa
anawandandalikira	anawaika m'magulu-magulu ankhondo
anawaswaiswa	anawaonongera kotheratu
anawawanya	anawaononga
anaweyula	ananyamula nsembe m'manja mwake ndi kuziyendetsa uku ndi uku kuzionetsa pamaso a Yehova
anawinda	analumbira
anayalika	anatandazya
anazisula	anapasula ndi kupanga cinthu cina
anazunzuka	ananyamuka mwamsanga
andilaka	andipambana, andigonjetsa
anditundudze	andibvutitse
angabuke	angapezeke, angaonetsedwe
angacete	angasoceretse
angalakike	angapambane, angagonjetse
angatikumike	angatikomane, angatilange
angokwalika	adzafa pang'ono-pang'ono
angothudzulidwa	angoonongedwa
ankharwe	ankhanza
ankhwenzule	anthu oipa aumbombo
ansinga	akapolo, andende
anhetemya	odziwa kuimba bwino
anthungo	anthu odziwa kucita nkhondo moponya mtundu wina wa mikondo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
apulukira	ali osadziwa, ali osamvera, ali olakwa
apululutsa	aononga kotheratu
asalende	asakhale ogwetsa manja pansu, asakhale osagwira nchito
asawinde	asalumbire
asazifukize	asapereke nsembe zonunkhira bwino
asumwa	acita mantha, acita cisoni
asungulumwa	akhala okha, ali opanda ciyembekezo
atafisula	atadya cakudya cam'mawa
atanda	ayenda mothamanga
atapira	atapita
atatsotsako	atakalirako kwa kanthawi, kukhala pa malo
atawafunkhira	atawabera mwankhanza
atawinda	atalumbira
aterafi	mafano
athangata	anthu amene anagwira nchito mosalipidwa cifukwa anakakamizidwa kucita tero ndi eni kapena mbuye wao
athudzuka	aonongeka
athundu	mitengo yolimba yokhala ndi moyo wautali onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a.
atibuke	aoneke, acokemo
atifunkha	atibera, atiiwira mwankhanza kapena moopseza, ationonga
atsonya	aonetsa kuti cocitikaco ndi coipa, azizwa
audio	munthu woipa, munthu wodetsedwa, wosapembedza
awafunkhe	awabere mwankhanza

ayaruka	apusa, asokonezeka
ayarukira	apusa, atengeka
azifukiza	apereka nsembe zonunkhira bwino
azifunyulula	azibvungulula zobvala zimene ziri zopeteka
azisule	apasule ndi kupanga cinthu cina
aziweyula	anyamula nsembezi m'manja mwake ndi kuziyendetsa uku ndi uku kuzionetsa pamaso a Yehova



B




bafuta	nsalu yofewa ya waiti
bande	njira, mapazi
bango	matete, bango imodzi ndiyo muyeso wa 2,67 - 3,30 meta
bati	muyeso wa 22 - 40 lita
bedola	zinthu za yelo kapena bulauni zimene zituluka m'mtengo ndi zonunkhira bwino
berulo	mwala wa buluu (blue) umene umaoneka monyezimira kwambiri
bini	muyeso wa 3,5 – 6,5 lita
bukitsani	falitsani, lemekezani
buli	mwezi wa Ayuda uli pakati pa October mpaka pakati pa November
bvuo	mtundu wa mbalame onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi b.
bvuwo	mtundu wa mbalame onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi b.
bwazi	comera cina cogwiritsidwa nchito kupanga zobvala onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi b.



C


cabwazi	comera cina cogwiritsidwa nchito kupanga zobvala, cingwe coyezera onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
cakupululutsa	cakuononga kotheratu
camkuwa	ca mwala wa kopa
camphwamphwa	colingana mu ufupi mwake ndi mu utali mwake
campwamphwa	colingana mu ufupi mwake ndi mu utali mwake
candamali	cida coonetsedwa kwa aliyense, cinthu cimene anthu afuna kulungamika
cansangalabwi	camwala (nthawi zina mwalawo ndi wokongola wokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana wolimba kwambiri)
caola	mliri, nthenda yoopsa kwambiri
cenjerere	tsitsi lalitali la nyama la mkango kapena kavalo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
ceza	kuunika
chemba	mpanda wa citetezo, zipupa zoteteza
chika	kansalu, bandeji, bedi, mphasa
chinga	cipupa, mpanda
cibakuwa	nsalu ya mtengo wapatali ya mtundu wa pepo
cibuluma	kukonza nthaka kuti ikhale omasuka
cidikha	malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
cidutsu	cidunswa
cifunkhidwa	caberedwa mwankhanza
cigono	msasa
cigwa	malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
cikhakha	monyoza ndi modzikweza
cikhato	pakati pa dzanja, muyeso wa 7,5 – 8,5 sentimeta kapena 22 – 25 sentimeta
cikomo	mwadzidzidzi, cinthu cobwera mosayembekezera
cikulaka	cikupambana, cikugonjetsa
cikunga	colingana, ciri monga
cikute	golide woumbidwa pamodzi
cikwi	sauzande (1000)
cikwirira	cibisala, cibvindikira, ciphimba
cikwiriritsa	ciphimbitsa, cibvindikiritsa
cilezi	ulesi, kona ya cobvala
cililaka	cilipambana, ciligonjetsa
cilimo	ulimi wa ku munda, masamalidwe a malo
cilindo	cipinda ca alonda ku munda
cimbalanga	mtundu wa dzombe
cimbwi	copfunda, nsalu, bulangeti
cimpepulo	kusowekeratu kwa ulemu
cinabuka	cinabuka
cinalizunguniza	cinalizungulira
cinapululutsa	cinaononga kotheratu
cinazomoledwa	cinang'ambidwa, cinaonongedwa
cindilaka	cindipambana, cindigonjetsa, cindibvuta
cinganga	kanthu kakang'ono ka neklesi (kobvala m'nkhosi)
cinkhanira	cimphanira onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
cinkhoma	mbuzi yokhala ku mapiri ndi yokwera ku maphiri
cinoni	nthenda ya pa masamba kapena pa zipatso kapena pa maphesi
cinsikwi	nthenda ya pa zomera
cinthenthe	kuopa, kunjenjemera ndi mantha kapena mkwiyo

ciombedwe	zinthu zimene ziikidwa pamodzi ndi kupanga cinthu cimodzi
ciphona	ngwazi, munthu wodziwa kumenya nkhole wosaopa
cipulukirire	kusadziwa, kusamvetsa
cipulukiro	kusadziwa, kusowa nzeru
ciputu	phesi youma, gaga, udzu youma
ciwidza	zamkati mwa nyama, ndowe
cirangali	lawi la moto
ciruli	cinthu cimene cinali kusewenzetsedwa posungiramo tirigu
cisabukenso	cisafalitsidwenso, cisapezekenso
cisanja	cisa ca mbalame
cisisira	nthawi yamene dzuwa lalowa kapena likalibe kuturuka, pamene pali mdima
cisumbu	malo ozunguliridwa ndi madzi mbali zonse
citando	ufupi wa cinthu
citipula	mbedi, mitundu ina ya kalimidwe
citowe	mbeu zomwe zimeretsa mbeu zogwiritsidwa nchito kukongoletsa cakudya
citsonyere	kuzizwa kwakukulu, kuonetsa kuti cocitikaco ndi coipa
citunda	phiri laling'ono
ciunda	malo yapamwamba imene wina aliyense akhoza kukuona
ciundo	polowera, pakhomu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
ciungwe	msonkhano wacisinsi
ciwinda	ngwazi, munthu wamphamvu wopambana
ciwindi	mphafa
ciwirire	kuphikidwa
cizirezire	nthawi imene dzuwa italowa komanso kusanade, kamdima kabwera, kulephera kuyang'ana bwino pamene uli ndi mabvuto
cizomoka	cing'amba, ciononga
cizomola	cing'amba, ciononga
cobukapo	cinthu cosayembekezeka koma caoneka
cofukiza	conunkhira bwino poperekedwa monga nsembe
cofunkha	cakuba
cofunkhidwa	cakuba, coberedwa mwankhanza
cokulakani	cokupambani, cokugonjetsani, cokulepheretsani
colalira	cocita udani, cobisala ndi colinga kukacita coipa
combo	cibwato cacikulu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi c.
comlaka	compambana, comgonjetsa
copululutsaco	coononga
cosafunkha	cimene sindinabe, cimene ndinaiwa lini
cosula	kupanga cinthu kucokera ku cidutsa cimodzi
cotsimphinaco	coyenda cociriwa
cotsonya	anthu ena azazizwa cifukwa ca cimene cinacitika kwa anzaa
cotsonyetsa	cinthu cozizwitsa, cinthu camanyazi
couluzidwa	otengedwa ndi mphepo, cosankhidwa bwino
couluzira	luwango
coundukula	ciapatso coyamba ca cokolola
cowinda	lumbiro
cowirikiza	kupereka cinthu moonjezera, kucita mopambana, kupereka cinthuco moonjezera m'mene iwe unacitira
cozokotera	cinthu camphamvu colimba kuti tingasemere pamwala
cozunguniza	cozungulira




D

dawi	mbeu zosafunika zonunkha
dinde	comera cina kapena mbeu yosafunika
dindiro	kamalo kakang'ono komangidwa m'minda komangidwa kuti anthu ayang'anire mbeu, malo yoyembekezera za m'munda
doko	gombe la nyanja, malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, malo kumene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi d.
dooko	gombe la nyanja, malo m'madzi osaya kwambiri kuti munthu angayendemo, malo kumene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi d.
dumbo	nsanje, zoipa ndi zosayenera, kuipa kuswa malamulo
dwale	malo opunthira tirigu kapena mphunga kapena cimanga onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi d.
dzandi dzandi	kukhala mosakazikika, kuyenda mosakhazikika (monga munthu woledzera)
dziputu	maphesi youma, gaga, udzu youma



E

efa	muyeso wa malita pafupifupi 20 - 45
efodi	cobvala copatulika ca wansembe wamkulu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi e.
eluli	mwezi wa Ayuda uli pakati pa August mpaka pakati pa September
etanimu	mwezi wa Ayuda uli pakati pa September mpaka pakati pa October



efodi

F


funkhani	ibani, iwani mwankhanza kapena moopseza, onongani
funkhitsa	amfunkhitsa

G

gudugudu	mtengo umene uli girini komanso uli ndi mayani ambiri
gumbwa	comera cacitali ndi coonda cimene cimamera m'mbali mwa madzi colingana ndi matete
guta	cobvala ca mtengo wapatali, cipupa
gwegwegwe	kulira kwa zoyendetsa zimene anali kugwiritsidwa nchito pa nkondo kapena ulendo

H

haleluya	lemekezani Yehova
hini	muyeso wa 3,5 - 7,5 lita
hisope	comera caubweya onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi h.
homeri	muyeso wa pafupifupi 220 lita



hisope

I

idabuka	idafalitsidwa
idafotero	mfumuyo inacita tero nthawi zonse
idafotsamira	mfumu inadalira pa munthuyo nthawi zonse
idamlaka	idampambana, idamgonjetsa
idzadziguwuda	idzadzimenya pa cifuwa
idzalalira	idzacita udani, idzabisala ndi colinga kukacita cinthu coipa, idzaononga
idzapululutsa	idzaononga kotheratu

idzasuka	idzatha
ikasula	ipasula, mbalame ipitikitsa ana ake
ikukha	itulutsa
ikunga	ili monga, ilingana
imso	makidini a nyama kapena a munthu, za m'kati mwa munthu, zinthu zabwino zambiri
inabuka	inafalitsidwa
inatanda	inakula
inatanda	inakula
inayalidwa	inatandazyidwa
ingadonthe	kucoka kwa madzi
ipotana	yolumikizana, yolukana
irikubuka	iri kuoneka, iri kuonetsedwa, iri kupezeka
itinthidwa	ikwezedwa mmwamba
iyangayanga	ikula mokumbatirana




K

kabawi	mtundu wina wa mbalame onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kadzakulakani	kadzakupambanani, kadzakugonjetsani, kadzakulepheretsani
kagumbwa	kacomera cacitali ndi coonda cimene cimamera m'mbali mwa madzi colingana ndi matete
kakasi	otaya ciyembekezo conse, osadziwa kucita ciani
kakombo	mtundu wina wake wa malawa onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kamphumphu	kanthunthu, kopanda cocotsapo, kopanda cocokapo
kamtanda	kabuledi kathunthu, fulawa yokanya
kanense	kakumo kakang'ono kothera
kansonga	kadutswa kakang'ono, kadutswa kakang'ono ka kothera kwa cinthu (monga khutu)
kapezi	inki ya m'colemba, nsalu ya redi m'kuwala kwake
kaphanthi	kamkate kosalala komanso koonda
kaphata	kuthamanga
katumbu	nyama ina imene ikhala m'madzi imadya nsomba
katungurume	mtundu wina wa cipatso monga kashonati onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kerubi	mtundu wina wa angelo
khali	mbali ina ya mkondo
khangaza	cipatso cimene cimaoneka ngati apulo kunja, koma ndi cacikulu ngati lalanje ndipo muli mbeu ngati granadila onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
khara	kamalasha kakang'ono ndiye kali ndi moto
khonje	comera cina colingana monga gavi onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
khunkha	mbeu zotsalira m'munda akamaliza kukolola
khwekhwe	msampha, ukuka, malo yobisika kupeza kuti ali colakwika ndipo colinga ca malo ajo ndi kuononga cinthu kapena munthu
khwisa	mbeu ina yosafunika m'munda
kida	cokongoletsa cakudya (monga sinamoni)
kinimani	cokongoletsa cakudya (sinamoni)
kisilevi	mwezi wa Ayuda uli pakati pa November mpaka pakati pa December
kofunyulula	kobvungulula
kondilaka	kondipambana, kondigonjetsa, kondilepheretsa
korale	cinthu camtengo wapatali ndipo nthawi zambiri cinali kusewenzetsedwa ngati codzikongoletsera
korali	cinthu camtengo wapatali ndipo nthawi zambiri cinali kusewenzetsedwa ngati codzikongoletsera
kori	muyeso wa 400 - 450 lita

kozokoteka	kolembedwa pa mwala mwa kusewenzetsa kusema
kubukitsa	kufalitsa, kukulitsa
kucezemira	kuwala kwakukulu
kucidikha	ku malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kucigono	ku msasa, ku malo pamene anali kukhala
kucigwa	malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kucitando	ku malo yaikulu
kucitunda	ku phiri laling'ono
kudololoka	kubvutika kwambiri kotero kuti alibe ciyembekezo
kudonthadontha	kulokwa pang'ono kwa mvula
kudooko	ku gombe la nyanja, ku malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, ku malo kumene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kudwale	ku malo opunthira tirigu kapena mphunga kapena cimanga onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kudzafunkha	kudzaba, kudzaiwa mwankhanza kapena moopseza, kudzaononga
kudzibukitsira	kudzikulitsira, kudzifalitsira, kudzipangitsira dzina
kudziguguda	kudzimenya pacifuwa ndi dzanja cifukwa ca cisoni
kudzikanda	kunyaula
kudzinyaza	kudzicititsa manyazi
kudzitakasika	kudzipulumutsa
kudzuma	kubuula, kulira kwambiri
kudzumanso	kubuulanso, kuliranso kwambiri
kufukiza	kupereka nsembe zonunkhira bwino
kufukizira	kupereka nsembe zonunkhira bwino
kufunkhidwa	kuberedwa mwankhanza
kufunyulula	kuonetsa
kuguguda	kucaya kwambiri, kugunda kwambiri
kuhahaza	kulira kwa nkondo
kuilaka	kuipambana, kuigonjetsa
kuiswaiswa	kuononga kotheratu, kuphwanya
kuiweyula	kunyamula nsembezi m'manja mwake ndi kuziyendetsa uku ndi uku kuzionetsa pamaso a Yehova
kukafukizira	kukapereka nsembe zonunkhira bwino
kukafunkha	kukaba, kukaiwa mwankhanza kapena moopseza, kukaononga
kukafwambira	malo oturukira utsi kapena cutsi
kukanda	kukanya
kukha	kutulutsa, kutaya kwa madzi am'thupi kosafunikira (mwacitsanzo kutaya magari nthawi yaitali kapena matenda opatsirana pogonana)
kukhathamiza	kugwetsa misozi pa mapazi ace, kukunanitsa ndi misozi
kukowa	kukasha cinthu cimene cifunika kucotsedwa
kukucetani	kukukopani, kukusoceretsani
kukunga	kukhala monga, kolingana
kukunkhulira	kukunkhuluka
kulakika	kupambana
kulalira	kubisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
kulinga	ku cipupa, ku mpanda, ku malo otetezeka
kulocapo	kusemapo
kulosa	kuulula zinthu zimene zifunika kukacitika m'tsogolo
kulunda	mkwiyo waukulu
kumakaliro	kothera kwa bwato
kumfukizira	kumperekera nsembe zonunkhira bwino
kumfumukira	kumuopa, kunjenjemera cifukwa ca mantha kapena ulemu, kupereka malo kwa wina
kumiraga	kumidzi, kumidzi yaing'ono
kumisanje	ku malo yokwezedwa, ku malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano

kumlalira	kucita udani, kubisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
kum'mero	kukamwa
kumpotosimpita	gulu lina la nyenyezi
kumsanje	ku malo yokwezedwa, ku malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
kumtompha	kumfufuzira
kumtsotsa	kumtsutsa
kumtundudza	kumuononga, kumbvutitsa
kumwirikizira	kupereka cinthu moonjezera, kucita mopambana, kupereka cinthuco moonjezera m'mene iwe unacitira
kunabuka	kunaoneka, kunaonetsedwa
kundilalira	kundicitira udani, kubisala ndi colinga kundicitira munthu wina coipa
kundipunza	kundinyoza, kundinyogodola
kundunji	kutsogolo, kutsogolo kumene umayang'ana
kunga	kolingana, ndi monga
kungaka	ku malo obisalamo, ku malo otetezeka, ku dzenje la nyama, ku malo obisalamo m'thanthwe
kunkhulirani	kunkhulukani
kunkhwangwala	malo yoonongeka, malo yamene yalibe cina ciriconse
kusinga	kundende
kunsonga	kothera kwa cinthuco, kothera kwa mitengo
kunyaza	kucititsa manyazi
kupaza	kupita pa njira yozungulira, kupitirira
kupsetsa mtima	kukwiyitsa, kukwiyitsa kwambiri
kupulukira	kusadziwa, kusamvera, kulakwa
kupululutsa	kuononga kotheratu
kupunzika	kunyozedwa
kusapota	kusapanga zobvala, kusasoka, kusaluka
kusawinda	kusalumbira
kusumwa	kucita mantha, kucita cisoni
kutsalima	kupindamuka, kuponya kwendo kumbuyo
kutsasa	kumsasa, kumisasa
kutsimphina	kuyenda cociriwa
kutsonya	kuzizwa, kuonetsa kuci cocitikaco ndi coipa
kutsotsa	kukhalirako, kukhala pa malo
kuukumika	kuutanthauzira, kukhala pafupi
kuukwirira	kuubisa, kuubvindikira
kuuna	polowera pa dzenje lakhumbidwa kwakuya
kuwalaka	kuwapambana, kuwagonjetsa
kuwasula	kuwapanga kucokera ku cidutsa cimodzi
kuwawawanya	kuwabera, kuwaononga
kuweyula	kunyamula nsembe m'manja mwake ndi kuziyendetsa uku ndi uku kuzionetsa pamaso a Yehova
kuwinda	kulumbira
kuyanja	cisomo, kulandiridwa mwaufulu mofikapo
kuyaruka	kupusa
kuzidikha	ku malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kuzigwa	malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi k.
kuzithando	ku misasa (ya nkondo)
kuzitunda	ku mapiri ang'ono
kuziwirikiza	kupereka cinthu moonjezera, kucita mopambana, kupereka cinthuco moonjezera m'mene iwe unacitira
kuzokota	kulemba pa mwala mwa kusewenzetsa kusema
kuzomotola	kung'amba, kuononga
kuzunguniza	kuzungulira
kuzurula	kuona fano losema koyamba



kwankharwe	kwankhanza, macitidwe ankhanza
kwete	malo ozungulira, kuzungulira, kuimira m'mbali-mbali
kwinda	funkha zobvala (kuti usagwe), peteka zobvala (mwacitsanzo ngati uli kuyenda pa madzi)
kwindani	funkhani zobvala (kuti musagwe), petekani zobvala (mwacitsanzo ngati muli kuyenda pa madzi)



L

lakitando	lalikulu m'ufupi mwake, lalikulu
lafunkhidwa	laonongedwa kwambiri
lagweregwere	guwa la nsembe m'mene mulibe kanthu m'kati koma yomangidwa kapena yosemedwa
lakhulo	dziko lopanda kanthu
lakudumana	tsiku lankhondo
lakudzafunkha	lakuononga
lakunga	lolingana, liri monga
lamkuwa	la mwala wa kopa
lamphwamphwa	lolingana mu ufupi mwake ndi mu utali mwake
lankhwenzule	laumbombo
lansangalabwi	lamwala (nthawi zina mwawo ndi wokongola wokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana wolimba kwambiri)
lende	lelembwela
libanika	kulira kwa lipenga kapena cofufuzera nthawi yaitali
libano	zomwe zimanunkhira poperekedwa monga nsembe
libukabuka	lioneke, lionetsedwa, lapezeka
lihawo	coteteza, cishango onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi l.
likabukitsidwe	likafalitsidwe
likole	cipinda pakati pa khomo lakunja ndi mkatikati mwa nyumba
likukha	litulutsa
likumika	likhala pafupi, lifikira

linabuka	linafalitsidwa, linapezeka, linakula
linabukitsidwa	linafalitsidwa
linafunyulula	libvungulula, lipangitsa
linalaka	linapambana, linagonjetsa
linamlaka	linampambana, linamgonjetsa
linawalaka	linawapambana, linawagonjetsa
linayalidwa	linatandazyidwa
linga	cipupa, mpanda, malo otetezeka
lingaka	coimbira cina cimene cikhoza kunyamulidwa poimba onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi I.
lipande	tumene tumakhala m'kati mwa tirigu (mbeu)
lirikubuka	liri kuoneka, liri kuonetsedwa, liri kupezeka
lisungulu	cida cimene cosewenzetsedwa potula khutu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi I.
litalunzika	litakazikika ndi kukhala ndi mphamvu monga mwa malamulo (pangano)
livyatanu	cinyama cacikulu ca m'nyanja onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi I.
lobuka	lioneka, laonetsedwa, lapezeka
lodikha	lamtendere, malo amtendere
lofukiza	lonunkhira bwino
lofunyulula	lobvungulula
lokowanidwa	lophatikizidwa
loluluka	losalemekezeka, laumphawi, losawerengedwa
lolunzika	lokazikika ndi lokhala ndi mphamvu monga mwa malamulo (pangano)
lopotana	lophatikizana, lolukidwa, lolumikizidwa
lopotapota	lophatikizana, lolukidwa, lolumikizidwa
losansitsa	zinthu zabwino, zofewa ndi zoyera zimene anagwiritsa nchito pa kupanga zobvala
lotakasuka	lopanda malire, lopanda malekezero, losatha
loweyula	lonyamulira zinthu m'manja ndi kuziyendetsa uku ndi uku kuzionetsedwa pamaso a Yehova
loyalika	lotandazyika
lozunguniza	lozungulira
lunguzi	comera cominga
luti	cida cogwirira ku mkondo



M

mabande	njira, mapazi
mabango	matete, bango imodzi ndiyo muyeso wa 2,67 - 3,30 meta
macawi	kusewenzetsa bwino nthawi ndi mpata yamene tapatsidwa

macemba	zipupa zozungulira midzi ndi zotetezera
madariki	dariki limodzi ndilo malipiro monga ndalama yopatsidwa pa tsiku
madoko	magombe a nyanja, malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, malo kumene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
madooko	magombe a nyanja, malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, malo kumene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
madwale	malo opunthira tirigu kapena mphunga kapena cimanga onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
magango	malo pamene pakumanizirana zinthu, kulumikizana kwa cinsalu, zinthu zolumikiza nsalu
magera	gera limodzi ndilo muyeso waung'ono wa 0,4 - 0,6 galamu
maguta	zipupa
mahomeri	homeri limodzi ndilo muyeso wa pafupifupi 220 lita
maiwe	madziwe ya madzi
makangaza	zipatso zimene zimaoneka ngati maapulo kunja, koma ndi zazikulu ngati maalanje ndipo muli mbeu ngati magranadila onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
makoma	zipupa
makongwa	mitambo yosonyeza kuti mvula iyamba posachedwa
makungu	mbali ya ziwalo zobisika za azimuna
malihawo	zoteteza, zishango onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
malimwe	nyengo yotentha
malinga	zipupa, mpanda, malo otetezeka
malingaka	zoimbira zina zimene zikhoza kunyamulidwa onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
malocedwe	masemedwe
maluli	luso
maluma	malo pamene pakumanirana zobvala za citsulo ca nkondo
malunga	kunjenjemera, kuopa kwambiri
maluti	zida zogwirira ku mikondo
mancedza	udzu womera m'madzi (monga machesi)
mangawa	ngongole
mankaka	makiyukamba onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mankhusu	gaga
maphaka	maziko ya zoikirapo zinthu
mapukusi	matumba ang'ono-ang'ono
marupiya	rupiya limodzi ndilo malipiro monga ndalama yopatsidwa pa tsiku
masafiro	miyala yamtengo wapatali
masalmo	nyimbo zacipembedzo
mase	cakudya cofewa copangidwa kucokera ku mkaka (chizi)
masekeli	sekeli limodzi ndilo muyeso waung'ono wa magalamu 10 mpaka 11.4 a siliva koma zinali za mtengo wapatali wofanana ndi malipiro a masiku anai
mastadiya	stadiya limodzi ndilo muyeso wa 185 – 192 meta
matalente	talente imodzi inali yofanana ndi muyeso wa makilogalamu pafupifupi 20 - 34 a siliva kapena golide, ndipo inali mtengo wa malipiro zaka 20 za nchito ya wanchito wamba
matamanda	madziwe ya madzi
matangadza	zomangira
matawale	madamu pokhala madzi
mathungo	malekezera
matomedwe	kuyamba kwa cikondi, cikondi coyamba
matsamvu	magulu a zipatso, mabalidwe ake amabala mounjikana pamodzi
matsango	magulu a zipatso, mabalidwe ake amabala mounjikana pamodzi


matsekerezo	zinthu zothandizira cinthu cimene anaika m'kacisi
maula	kufufuza za umoyo mwacitsanzo mwa kupita ku ng'anga kapena anthu a mizimu yoipa
mavwendi	mavwemba (mawatemeloni)
mazana	mahundredi (100)
mazenga	majeko
mazokotedwe	masemedwe
m'bande	m'njira
mbano	zida zazing'ono zagolide zimene zinagwiritsidwa nchito kudula zidutswa zoyaka kale za nyali kapena kandulo, mipiringidzo yopingasa yoikapo zinthu za m'kacisi
mbawa	mtundu wa mbalame zazing'ono monga thaki
mbetete	mtundu wina wa malipenga kapena zoimbira kapena zofufuzera
mbinyiru	kothera kwa cobvala
mbudulira	nthawi ya manyazi yako
mbulu	matenda omwe mimba imatupa, m'kati mwa cipatso ca nkhuu yakhala monga mankhwala
m'cenje	mbiya yaing'ono, mbiya yaikulu
mcerenje	mtsinje, njira mopita madzi
m'cidikha	m'malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'cigono	m'msasa
m'cigwa	m'malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'cimpuli	m'poto
m'cirangali	m'lawi la moto
m'cirezire	nthawi imene dzuwa italowa komanso kusanade, kamdima kabwera, kulephera kuyang'ana bwino pamene uli ndi mabvuto
m'ciruli	m'cinthu cimene cinali kusewenzetsedwa posungiramo tirigu
mcisu	mitengo yonunkhira bwino yokhala ndi maluwa ang'ono-ang'ono oyera onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'citando	m'ufupi mwake
m'citunda	m'phiri laling'ono
m'doko	m'gombe la nyanja, m'malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, m'malo m'mene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'dumbo	m'nsanje, m'zoipa ndi zosayenera, m'kuipa kuswa malamulo
mfula	mtundu wina wa cipatso monga kashonati, nthawi ya manyazi yako onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mgwalangwa	mitengo womera ku malo otentha umene ukula kopanda nthambi koma kothera kwake kumakhala nthambi ndi masamba ambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
micenje	mbiya zazikulu
mifula	mtundu wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
migwalangwa	mitengo yomera ku malo otentha imene ikula kopanda nthambi koma kothera kwake kumakhala nthambi ndi masamba ambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
miimba	mbalame zolusa zokudya nyama monga mbewa kapena nyama zakufa kapena mbalame zina onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mikawo	zinthu zocititsa manyazi
mikoli	ukapolo, am'ndende
mikono	mkono umodzi ndi muyeso wa 44 – 52 sentimeta
mikungudza	mitengo ya mtundu wina imene ili yaikulu ndi yolimba komanso imene imakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mikunkhu	zitsulo zomenyera munthu


mikwamba	muyeso (mikwamba makumi awiri ndiyo muyeso wa 36 meta ndipo mikwamba khumi ndi isanu ndiyo muyeso wa 27 meta)
miliu	tunthu tolira twatung'ono-tung'ono pamene munthuyo ayenda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
milulu	zomera zazitali ndi zoonda zomera m'mbali mwa madzi zolingana ndi matete onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
miomba	mikondo yogwiritsidwa nchito posodza nsomba
mipambo	magulu-magulu ya nkondo, magulu-magulu ya miyala
mipango	zomangira zopangidwa ndi nsalu, mabeluti yansalu
mipikizo	zitsulo zina zimene zinagwiritsidwa poletsa anthu kutsegula citseko
miraga	midzi, midzi yaing'ono
mirimo	zinthu zofunikira zomangira
misanje	malo yokwezedwa, malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
misiwe	mapaipi
misona	ana a mikango, mikango yaing'ono
misonododzi	mitengo yomwe imamera m'mbali mwa mitsinje onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mitanda	mbale ya cakudya, fulawa yokanya, keke kapena buledi yathunthu, pulanga lalikulu, cogwirira ca mawilo
mitawi	nthambi
mitsindo	nchafu za m'miyendo
mitsita	m'nchafu za mapazi ya akavalo
mitungo	mafoloko yaikulu yogwiritsidwa nchito pa kuphika nyama
mitungwi	mtundu wa minga
mizaza	mtundu wa nchenche monga kamzembe
m'kakolo	malo pamene pali madzi yocepa muyeso wake khumbira phazi
mkandankhuku	mtengo wina, mtengo wa malubeni
mkawo	zinthu zocititsa manyazi
mkhungu	munthu wakuba, munthu woipa
m'khwekhwe	m'msampha, m'ukuka, m'malo yobisika kupeza kuti ali colakwika ndipo colinga ca malo ajo ndi kuononga cinthu kapena munthu
mkombero	zinthu zimene zionetsa cinthuco kukhala cokometsetsa (mwacitsanzo msiro), malo otetezera cinthu cina
mkono	muyeso wa 44 – 52 sentimeta
mkundi	mtundu wina wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mkungudza	mtengo wa mtundu wina umene uli waukulu ndi wolimba komanso womwe umakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mkunkhu	citsulo comenyera munthu
mkuntho	mphepo yaikulu
m'kupsetsa mtima	m'kukwiya kwambiri
m'kupulukira	m'kusadziwa
m'kusomphoka	m'kotalika kwace kwa cinthuco
mkuwa	mwala wa kopa
mlalang'ambwa	gulu lina la nyenyezi
mlangali	zobvala zamtengo wapatali za redi
mlauli	anthu a Mulungu amene anena za m'tsogolo
mlezo	nsalu yomwe imagwiritsidwa nchito pomangira mutu munthu wakufa (mtembo)
m'litsipa	m'mbali mwa mutu popanda mafupa pafupi ndi maso
mliu	kanthu kakang'ono kolira pamene munthuyo ayenda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mlombwa	mtundu wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mlubza	kusayang'ana cina cake
mlulu	comera cacitali ndi coonda comera m'mbali mwa madzi colingana ndi matete onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'mabande	m'njira

m'mabango	m'matete
m'macinga	m'mipanda
m'madwale	m'malo opunthira tirigu kapena mphunga kapena cimanga onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'magango	m'malo pamene pakumanizirana zinthu, kulumikizana kwa cinsalu, m'zinthu zolumikiza nsalu
m'makoma	m'zipupa
m'malinga	m'zipupa, m'mpanda, m'malo otetezeka
mmaliwongo	munthu wotsutsana naye
m'mapanthi	malo yamene amaikapo zinthu za m'kacisi, malo ocepa amene anali kuthandizira zoikapo za m'kacisi
m'matangadzamo	m'zomangiramo
m'matsekerezo	m'malo kothera kwa mzinda
m'mero	m'kamwa, m'kati mwa m'kamwa
m'miraga	m'midzi, m'midzi yaing'ono
m'misanje	m'malo yokwezedwa, m'malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
m'mkawo	zinthu zocititsa manyazi
m'molalira	m'malo mobisalamo ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
m'mwamvu	nyengo yamvula
m'ngaka	mu malo obisalamo, mu malo otetezeka, m'dzenje la nyama, mu malo obisalamo m'thanthwe
m'ngudulira	m'mkhanjo
m'nsinga	m'maunyolo
m'nsonga	m'kothera kwa nthambi
m'nsupa	m'botolo (mosungiramo mafuta)
mofunkha	mwa kuba, mwa kuiwa mwankhanza kapena moopseza, moononga
mokwiririka	malo mobisaliramo
momlalira	mocita udani, mobisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
mopazapaza	mopita pa njira yozungulira
motakasuka	ku malo abwino kuti munthu amasuke ndi kupeza mtendere
motapira	kutenga malo kupatsa mapfuko kapena mitundu
motsetsereka	malo yakuya kwambiri, malo otseruka kwambiri
mowirikiza	kupereka cinthu moonjezera, kucita mopambana, kupereka cinthu moonjezera m'mene iwe unacitira
moyalidwa	motandazyidwa
moyalika	motandazya
moyaruka	monga munthu wocita misala, munthu wopusa, mosokonezeka
mpalu	wodziwa kusaka bwino kwambiri
mpambo	mizera ya mitengo
mpango	comangira comangidwa ndi nsalu, beluti yansalu
mpepulo	kusowekeratu kwa ulemu
mpfuno	mphuno
mphala	zinthu zopanda nchito
mphalasa	citoliro colingana ndi lipenga kapena cofufuzera onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mphambu	kupatikana kwa cinthu cina ndi cina
m'phamphu	m'cifundo cocokera pansi pamtima
mphande	zokongoletsera zomwe anthu amabvala zooneka ngati miyezi yaying'ono
mphanthi	m'mabvuto, anthu ozunzidwa
mpherere	kulonjeza cinthu cina
mphero	mwala umene anali kusewenzetsa masiku akale pa kugaya kapena kupera zinthu
mpheta	kambalame kakang'ono, timbalame tating'ono
mphindo	cida cina ca makina comwe cinayenda mofulumira popanga zobvala
m'phodo	monyamuliramo mikondo
mphodza	mtundu wa nyemba
mphoka	mafuta onunkhira, mtengo wosewenzetsedwa pa kupanga mafuta onunkhira


mphonje	kotoni yolukidwa imene Aisrayeli anamangirira ku zobvala zao ngati zizindikiro ndi zikumbutso kukumbukira malamulo a Mulungu ndi kuwatsatira tsiku ndi tsiku onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mphoyo	nyama zina onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mphuci	mtundu wina wa dzombe
mphulumukwa	zomera zimene zikula mwacilengedwe popanda kulimidwa
mphungu	mbalame ina yolusa, munthu wopatsa uphungu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mphuthu	felemu ya citseko, pakhomu
mpikizo	citsulo cina cimene cinagwiritsidwa poletsa anthu kutsegula citseko
mpiringidzo	kabale
mpokolowekapo	podalira pa zonse
mpumo	mpweya
msanje	malo yokwezedwa, malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
msona	mwana wa mkango, mwana wa njati, mkango waung'ono
msondodzi	mtengo womwe umamera m'mbali mwa mitsinje onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
msongwe	kukhala patsogolo
msundu	nyongolotsi ya m'madzi yodziphatika ku thupi la munthu kuti ikayamwe magari ya munthuyo
mtambasali	kukhala okondwa ndi mopanda kukomana ndi bvuto ina iliyonse
mtanda	mbale ya cakudya, fulawa yokanya, keke kapena buledi yathunthu, pulanga lalikulu
mtanda woombera nsaru	kamtanda kolemera ka makina yomwe inagwiritsidwa nchito kusoka zobvala onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mtanthanyerere	zonunkhira bwino,
mthendene	siketi yomwe ndi yaitali
mthonzo	kunyoza, kudzudzula
mtobvu	citsulo cofewa cosachedwa kusungunuka
m'tsango	m'gulu la zipatso, mabalidwe ake amabala mounjikana pamodzi
m'tsenjezi	m'kati kwambiri
mtsonyo	kuzizwa, kuonetsa kuti cocitikaco ndi coipa
mtulo	mphatso
mtungwi	mtundu wa minga
mudzafunkhe	mudzabere anthu ena mwankhanza
mudzifunkhire	muiwe kuti mukhale nazo zakuba
mufisule	mudye cakudya cam'mawa
muimba	mbalame yolusa yokudya nyama monga mbewa kapena nyama zakufa kapena mbalame zina onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mukalakike	mukapambane, mukagonjetse
mukukha	muturutsa
mulikutunsika	muli kuthawa kucokera kwa Mulungu
mumkumika	mukhala pafupi naye, mukomana naye
mumkuntho	mumphepo yaikulu
mumlaka	mumpambana, mumgonjetsa
mumphandumo	m'kuukira
munabwadamuka	munazizira, munalira
munadzibukitsira	munafalitsa za inu nomwe, munadzikweza
munailaka	munaipambana, munaigonjetsa
mundipembere	mundipempherere
mundiyalikira	munditandazyire, mundikonzekere
mungu	gaga, udzu youma
muomba	makina ogwiritsidwa nchito polumikiza makotoni kukhala nsalu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
mure	conunkhira bwino poperekedwa monga nsembe
musafukiza	musapereke nsembe zonunkhira bwino

musakwirira	musabise, musabvindikire
musamapulukiranso	musakhalenso osadziwa, musakhalenso osamvera
musamapunamiza	musatseke pakamwa pa ng'ombe
mutsetsepo	mukhalireko, muyembekezeko
muula	mtengo wa apulo
muwirikize	kupereka cinthu moonjezera, kucita mopambana, kupereka cinthuco moonjezera m'mene iwe unacitira
mvunja	mankhwala onunkhira bwino makamaka poperekedwa monga nsembe
mwafukiza	mwapereka nsembe zonunkhira
mwalakika	mwapambana
mwamlaka	mwampambana, mwamgonjetsa
mwamvu	nyengo yamvula
mwaniko	ndi dzina la malo yoyenderamo, dzina la njira
mwankharwe	mwankhanza
mwanthuku	mosaganizira
mwayaruka	mwacita misala, mwapusa
mweya	mpweya
myundo	mvula yoyamba
m'zidikha	m'malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'zidundumwa	m'makhomo, m'zipinda pakati pa khomo lakunja ndi mkatimkati mwa nyumba
m'zigologolo	m'maunyolo
m'zigono	m'misasa
m'zigwa	m'malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'zikwakwata	m'masandasi, m'masilipa onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi m.
m'zitando	m'misasa (ya nkondo)
m'zithando	m'misasa (ya nkondo)
m'zitunda	m'mapiri ang'ono
mzukwa	maonekedwe a thupi la munthu koma siioneka bwino kotero kuti anthu angaganize kuti ndi mzimu







mphoyo



mphungu



msondodzi/misondodzi




mkundi




mphalasa



mlulu/milulu



mgwalangwa/migwalangwa



mfula/mifula




mcisu




mlombwa



m'cigwa/m'zigwa




malihawo



mkungudza/mikungudza




mankaka



makangaza



madwale/m'madwale



mliu/miliu



madoko/m'doko/madooko






N

nabukitsa	nafalitsa, kufalitsa
naceta	nasoceretsa, kusoceretsa
nadzafunkha	nadzaba, nadzaiwa mwankhanza kapena moopseza, nadzaononga, kudzaba
nadzakunkhulira	nadzakunkhuluka, kudzakunkhuluka
nadzawalaka	nadzawapambana, nadzawagonjetsa, kudzapambana
nadzifunkhira	naiwa mwankhanza kuti akhale nazo zakuba, kuiwa mwankhanza
nadziguguda	nadzimenya pacifuwa ndi dzanja cifukwa ca cisoni, kudzimenya pa cifuwa
nadzithinula	nayondoloka, nadzithamvunula
nafukiza	napereka nsembe zonunkhira bwino, kupereka nsembe zonunkhira bwino
nafukize	napereke nsembe zonunkhira bwino, kupereka nsembe zonunkhira bwino
nafukizira	napereka nsembe zonunkhira bwino, kupereka nsembe zonunkhira bwino
nafunkha	nakuba, naiwa mwankhanza kapena moopseza, naononga, kuiwa
nafunkhire	nabera mwankhanza, kubera mwankhanza
naifukizira	naipereka nsembe zonunkhira bwino, kuipereka nsembe zonunkhira bwino
nakamlaka	nakampambana, nakamgonjetsa, kukapambana, kukamgonjetsa
nakanda	nakanya, naponya, kukanya, kuponya
nakwirira	nabisa, nabvindikira, kubisa, kubvindikira
nakwiriridwa	naphimbidwa, nabvindikiridwa, kuphimbidwa, kubvindikiridwa
nalakika	nagonjetsa, kugonjetsa
nalalira	nacita udani, nabisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa, kucita udani
nalenjeka	nakoloweka, kukoloweka
nalithudzula	naliononga, kuliononga
nalosa	naulula zinthu zimene zifunika kukacitika m'tsogolo, kuulula za m'tsogolo
namfunyulula	nabvungulula kalata limene liri lopeteka, kubvungulula
namlalira	namcitira udani, nabisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa, kumcitira udani
namperetsa	nampangitsa kukhala wogaya, kumpangitsa kukhala wogaya
nandandalika	nakhala m'magulu-magulu ankhondo, kukhala m'magulu-magulu ankhondo
nandandalitsa	nakhaliitsa m'magulu-magulu ankhondo, kukhalitsa m'magulu-magulu ankhondo
nandengulitsa	nagwedeza dziko, kugwedeza dziko
nandipululutsa	nandiononga kotheratu, kundiononga kotheratu
nangula	citsulo colemera coletsa kusuntha kapena kuyenda kwa bwato onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
nanika	kuika asirikali kuti akhala okonzeka kucita nkhondo
naphazira	nayenda njira yozungulira, kuyenda njira yozungulira
naphini	mtundu wina wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
napululutsa	naononga kotheratu, kuononga kotheratu
nardo	mafuta odzola amtengo wapatali komanso onunkhira bwino opangidwa kuchokera ku mizu ya comera
nasasatulira	nakweza manja ake kumwamba, kukweza manja kumwamba
naseama	kukhala pansa mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
nasumwesumwe	nakhala odabwa ndi mantha, kukhala odabwa ndi mantha
natanda	nakula, kukula kwa nkhondo
natilalira	naticitira udani, nabisala ndi colinga kukaticitira coipa, kuticitira udani
natsotsa	nakhalirako, kukhala pa malo

natundudzidwa	nabvutitsidwa, kubvutitsidwa, kuonongedwa
naufunyulula	nabvungulula buku limene liri lopeteka, kutsegula buku
naukanda	naukanya, kukanya
nauzunguniza	nauzungulira, kudzungulira
nawabukitse	nawafalitse, kulankhula
nawalaka	nawapambana, nawagonjetsa, kupambana
nawamoza	nawapyoza, kulasa ndi nkondo, kuwapyoza
nawapolonganitsa	nawasokoneza, kuwasokoneza
nawinda	nalumbira, kulumbira
nazikwirira	nazibisa, nazibvindikira, kuzibis
naziweyula	kunyamula nsembezi m'manja mwake ndi kuziyendetsa uku ndi uku kuzionetsa pamaso a Yehova
nazunguniza	nazungulira, kuzungulira
nazunzuka	nanyamuka mwamsanga
nchetho	mtundu wina wa mikondo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
ncinci	cakudya cofewa (keke) copangidwa ndi cipatso ca nkhuu, cakudya cofewa copangidwa ndi zocokera ku mkaka
ndafunyulula	ndapanga kumwamba kuti ioneke
ndakapiza	ndawaza mafuta onunkhiritisa
ndakubukitsira	ndakufalitsira
ndalalira	ndabisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
ndalilaka	ndalipambana, ndaligonjetsa
ndamceta	ndamsoceretsa
ndamlaka	ndampambana, ndamgonjetsa
ndapukwa	ndakhala okonzeka
ndasonthokera	ndanena mau acabe
ndibukitse	ndifalitse
ndidafopita	ndinapita nthawi zonse
ndidzabukitsa	ndidzautsa
ndidzadzikuzitsa	ndidzadzioneketsa cacikulu, ndidzadzikulitsa
ndidzakufukizirani	ndidzakuperekerani nsembe zonunkhira bwino
ndidzakukhathamiza	ndidzakunyowetsa, ndidzakunanitsa ndi misozi
ndidzakukowa	ndidzakugwira ndi kukoka iwe
ndidzakutomera	ndidzakukatira
ndidzalalira	ndidzacita udani, ndidzabisala ndi colinga kukacita coipa
ndidzaloca	ndidzasema, kusema
ndidzambukitsa	ndidzamlemekeza, ndidzafalitsa za iye
ndidzasasatulira	ndidzakweza manja kumwamba
ndidzatonyola	ndidzanyoza
ndidzatunsa	ndidzacotsa
ndidzawalaka	ndidzawapambana, ndidzawagonjetsa
ndikamlaka	ndikampambana, ndikamgonjetsa
ndikunga	ndiri monga, ndilingana
ndinadzitomera	ndinadzikatira
ndinasumwa	ndinacita mantha, ndinacita cisoni
ndinawinda	ndinalumbira
ndipembere	ndipempherere inu
ndipumpuntha	ndilangiza, ndiletsa
ndiwakumika	ndikhala pafupi nao, ndiwapeza
ndolo	mtundu wina wa citsulo cofewa (wolingana ndi sodaling'i waya)
nduwira	duku, cophimba mutu comwe anthu makamaka ansembe a Yehova anabvala pa mitu yao onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
ngaho	zonunkhira, zokongoletsa cakudya
ngaka	malo obisalamo, malo otetezeka, dzenje la nyama, malo obisalamo m'thanthwe
ngalande	mitsinje ya madzi

ngale	zinthu zodula zolimba ndi zowala ndizo zopangidwa ndi nyama za m'madzi ndipo nthawi zambiri zimagwiritsidwa nchito popanga zodzikongoletsera
ngowe	cida cooneka monga cifuloko cacikulu cimene cinasewenzetsedwa kuphika nyama
ngudulira	mkhanjo
ngwopulukira	ndi wosamvera, ndi wolakwa, ndi wosadziwa
nibukanso	kuonekanso, kupezekanso
nicidzalaka	nicidzapambana, nicidzagonetsa
nidontha	kungena kwa madzi
nika	kuika asirikali kuti akhala okonzeka kucita nkondo
nikapakapa	kuuluka pamwamba pa tuwana twa mbalame
nilindipfundukira	kucoka kwa khungu
nimukaceteka	mukasoceretsedwa
nimundipembere	mundipempherere
nimusumwe	kukhala odabwa ndi mantha
nisana	mwezi wa Ayuda uli pakati pa March mpaka pakati pa April
niumatira	kuufungatira
niwalaka	kuwapambana, kuwagonjetsa
njera	kuimiratu konse
njeresa	cinthu copangidwa mwa kutentha miyala ina yapadera ndipo cinthuco cinasewenzetsedwa monga pulasta
njereza	cinthu copangidwa mwa kutentha miyala ina yapadera ndipo cinthuco cinasewenzetsedwa monga pulasta
njirisi	zingwe za blaki ndi tumabokosi zimene azimuna a m'Israyeli anabvala pamutu ndi pamanja popemphera ndipo momwemo munali tumapepala tolembedwapo mau a m'Baibulo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
njombi	magulu a tsitsi la munthu kapena tsitsi loluka
nkanambo	khungu loonongeka
nkhafi	ndodo zogwiritsidwa nchito poyendetsa bwato
nkhanambo	zilonda, khungu loonongeka
nkharwe	nkhanza
nkholo	kothera kwa ng'ombe
nkhwimba	mapanga m'miyala mwakuya kwambiri
nsadwa	gaga
nsambo	makotoni
nsangalabwi	mwala (nthawi zina mwalawo ndi wokongola wokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana wolimba kwambiri)
nsangwe	gulu lina la nyenyezi
nsanje	kaduka, zoimbira zina onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
nsapule	mtundu wina wa mphete wa ku matu
nsenga	zokhalira pansu m'kapu (votikama) ndipo nthawi zina ziimirira mkwiyo wa Mulungu, anthu okudya zonse osasiya kanthu
nsenye	kutayika kwa pakati
nsici	mizati, mapilala
nsinga	maunyolo
nsonga	kothera kwa cinthuco
nsupa	botolo, mabotolo makamaka osungiramo mafuta
nthubwinthubwi	nyanja yozama
nthungo	mtundu wina wa mikondo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
nthyole	nthambi
nubukitse	nufalitse
nufukize	nupereke nsembe
nukamkumike	nukakumane naye, kukampeze
nukwirira	nubisa, nubvindikira
nulocepo	nusemepo

numgola	numusautsa
numpidigula	numpindamula
nungu	mtundu wina wa nyama onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
nusu	hafu, kadunswa ka cinthu cina cake
nuukungudza	nuudya konse
nuwacanutse	nuwaseme
nyengo yacisanu	nyengo yozizira
nyondonyondo	mafunde amphamvu
nyonga	mphamvu, mwamphamvu
nyung'unyu	fupa la m'ciuno
nyuru	kavalo ndi bulu atakwererana akabala mwana mwanayo ndiye achedwa nyuru onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi n.
nzera	magulu a tsitsi limene likulira pamodzi



O



odikha	amtendere
odzithinula	anthu oyondoloka, odzithamvunula
ofukizira	anthu opereka nsembe zonunkhira bwino
ofunkha	anthu akuba, anthu oiwa mwankhanza kapena moopseza, anthu oononga
ofunkhidwa	oberedwa mwankhanza
ojinca	athanzi ndi amphamvu
okambululudwa	opanda mphamvu, oopyezedwa
okumika	otanthauzira mwambi, okhala pafupi
okwinda	ofunkha zobvala (kuti musagwe), opeteka zobvala (mwacitsanzo ngati muli kuyenda pa madzi)
olakika	anthu opambana m'nkondo, ogonjetsa
olalira	obisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
olama	abwino, athanzi, opatsa thanzi, omveka bwino

olocedwa	osemedwa
olosa	anthu amene anenera, anena za m'tsogolo
oluluka	osalemekezeka, aumphawi, osawerengedwa
olunzika	ogwirizana
omlalira	omcitira udani, obisala ndi colinga kukacitira munthu wina coipa
ondandalikira	anthu okhala m'magulu-magulu ankhondo, okonzeka kucita nkhondo
ondilalira	ondicitira udani, obisala ndi colinga kukandicitira coipa
openduza	anthu okhala pafupi ndi mizimu yoipa, anthu amatsenga
opinduka	anthu amitundu amene adatembenukira kwa cipembezo ca Ciyuda (ca Aisrayeli)
opota	ophatikizana, olukidwa, olumikizidwa
opulukira	osadziwa, osamvera, olakwa
opulupudza	ouma mtima, otsutsa, osamvera, oipa
osafukizanso	osaperekanso nsembe zonunkhira bwino
osawakumika	osakhala pafupi nao
osula	anthu odziwa kupanga cinthu kucokera ku cidutswa cimodzi, anthu odziwa kupasula ndi kukhoma cinthu cina
osusuka	osakhutira, odyerera, opanda malire
otilaka	otipambana, otigonjetsa
otsimphina	oyenda cociriwa
otyasika	onyenga, abodza
owalalira	owacitira udani, obisala ndi colinga kukawacitira coipa
owawanya	anthu oonongera, akawalala
owirikiza	kucita mopambana
oyaruka	opusa, osokonezeka
ozerevera	okhala okonzeka kucita cinthu, ofuna
oziya	acisoni
ozunguniza	ozungulira

P

pacandamali	pa cida coonetsedwa kwa aliyense, pa cinthu cimene anthu afuna kulungamika
pachika	pa bedi, pa mphasa
pacidikha	pa malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
pacigono	pa msasa
pacigwa	pa malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
pacitowe	pa mbeu zomwe zimeretsa mbeu zogwiritsidwa nchito kukongoletsa cakudya
pacitunda	pa phiri laling'ono
paciundo	polowera, pakhomo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
pacothwikira	cida cakuthwa cimene bulu kapena ng'ombe sakhoza kuponya kwendo yake kumboyo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
padagu	malisece, kotseguka
padooko	pa gombe la nyanja, pa malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, pa malo pamene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
padwale	pa malo opunthira tirigu kapena mphunga kapena cimanga onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
padzayalidwa	padzatandazyidwa
pagwangwa	pa malo pamene pagwirizirana mafupa a mapewa ndi dzanja
pakumkumika	pakukhala pafupi naye, pakumupeza
pakutsimphina	pakuyenda cociriwa
pakutsotsa	pakupuma kwa kanthawi, pakukhala pa malo
palikole	pa cipinda pakati pa khomo lakunja ndi mkatikati mwa nyumba
palinga	pa cipupa, pampanda, pa malo otetezeka

palitsipa	pa mbali mwa mutu popanda mafupa pafupi ndi maso
palukani	patukani
pamadooko	pa magombe a nyanja, pa malo osaya kwambiri m'madzi kuti munthu angayendemo, pa malo pamene maboti amafika kumtunda onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
pamakoma	pazipupa
pamatamanda	pa madziwe ya madzi
pambinyiru	kothera kwa zobvala
pamisanje	pa malo yokwezedwa, malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
pamitanda	pamapulanga atali
pammero	pakamwa pao
pamsanje	pa malo yokwezedwa, pa malo yokwezedwa kumene anthu anapembedza mafano
pamtanda	papulanga lalikulu
pamtungwi	pa mtundu wa minga
panayalidwa	panatandazyidwa
pandunji	kutsogolo, kutsogolo kumene umayang'ana
panduwira	pa cophimba mutu comwe anthu makamaka ansembe a Yehova anabvala pa mitu yao onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
pangaka	pa malo obisalamo, pa malo otetezeka, pa dzenje la nyama, pa malo obisalamo m'thanthwe
pangalande	pamitsinje ya madzi
pansenga	pa zokhalira pansi m'kapu (votikama) ndipo nthawi zina ziimirira anthu opezeka m'zinthu zabwino zokha-zokha (mtendere)
pansinga	pa malo pamene tidonsera uta kuti tiuponye
pansonga	pothera, pamwamba
paphaka	pa mapulanga yoyenda pamadzi monga bwato
paphalo	polumikizira phewa ndi dzanja la phewa
pathawale	padamu ya madzi
pathundu	pa mtengo wolimba wokhala ndi moyo wautali onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
patsinde	munsi mwa mtengo
pazidundumwa	pazipinda pakati pa khomo lakunja ndi mkatimkati mwa nyumba
pazitunda	pa mapiri ang'ono
paziundo	polowera, pakhomo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi p.
pazofunkha	pazakuba, pakuononga
peni	colembera
peyupeyu	kukhala wofooka kwambiri kuti usayende bwino, kuyenda mogwedezeka
phaka	maziko ya zoikirapo zinthu
phamphu	cifundo cocokera pansi pamtima
phanthiphanthi	cidutswa cosalala komanso coonda
phodo	monyamuliramo mikondo
phoso	cakudya, cakudya ca pamseu, zofunika pa umoyo
pobuka	pofalitsidwa
pofukizira	popereka nsembe zonunkhira bwino
polifunyulula	polibvungulula
pomkumika	pokhala pafupi naye, pomupeza
poomberapo	mopanda bvuto monga munthu wosoka amadula kotoni
popaza-paza	popita pa njira yozungulira, popitirira
potakasa	pogwedeza kwakukulu, pogwendeza nthawi yaitali
potsetsereka	poyenda pa malo otseruka kwambiri
potsetseremba	malo otseruka kwambiri, malo akuya kwambiri
potsimphina	poyenda cociriwa
poyalidwa	potandazyidwa
pwepwete	kuseka mosekera, kuseka monyogodola, kuseka kwambiri




S

sadzalakika	sadzapambana, sadzagonjetsa
sadzaulaka	sadzaupambana, sadzaugonjetsa
sadzausula	sadzaupasula, sadzauononga
safiri	mwala wa mtengo wapatali
safiro	mwala wa mtengo wapatali
sakunga	sali monga, salingana
salimo	nyimbo yacipembedzo
salmo	nyimbo yacipembedzo
sanakukumikani	sanakhale pafupi ndi inu, sanakumane ndi inu
sanamlaka	sanamgonjetse
sanandilaka	sanandipambane, sanandigonjetse
sapota	sapanga zobvala, sasoka, saluka
segati	mwezi wa Ayuda uli pakati pa January mpaka pakati pa February
sekeli	sekeli limodzi ndilo muyeso waung'ono wa magalamu 10 mpaka 11.4 a siliva koma zinali za mtengo wapatali wofanana ndi malipiro a masiku anai
sera	cinthu cimene cimasungunuka mosabvuta monga khendulo
sicinalakika	sicinapambane
silikulakani	si lobvuta kwa inu, si lalikulu kwambiri
simukadakumika	simukadakhale pafupi, simukadatanthauzire
sinamoni	cokongoletsa cakudya
sitidawafumukira	sitinawaope, sitinawapereke malo
sitinyanyampiradi	sitidzikulitsa moponda malire
sivani	mwezi wa Ayuda uli pakati pa May mpaka pakati pa June
sohamu	mwala wamtengo wapatali
sudzadzomboleredwa	sudzathenuliridwa
sudzamlaka	sudzampambana, sudzamgonjetsa
sula	panga, khoma

sulfure	mitundu ina ya miyala ya yelo ndi yamoto
sundwe	zogonera kapena zokolola za caka catha

T

tafunkhidwa	taonongedwa kwambiri, taberedwa mwankhanza
talente	talente imodzi inali yofanana ndi makilogalamu pafupifupi 20 - 34 a siliva kapena golide, ndipo inali mtengo wa malipiro zaka 20 za nchito ya wanchito wamba
tandaude	kangaude
tantha	nakugwa thupi lonse
taphanthi	timikate tosalala komanso koonda
taphanthipanthi	timikate tosalala komanso koonda
tebete	mwezi wa Ayuda uli pakati pa December mpaka pakati pa January
thadzi	nkhuku
thangata	nchito yosalipidwa, msonkho wina
thawale	damu ya madzi
thonzo	kunyoza, kunyozedwa
thundu	mtengo wolimba wokhala ndi moyo wautali onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi t.
thungo	malekezere, malire
tidzamlaka	tidzampambana, tidzamgonjetsa
tikafunkhe	tikaiwe mwankhanza
tilakatu	tipambana ndithu, tigonjetsa ndithu
timalinga	tizipupa, timpanda, timalo totetezeka
timitanda	timakeke kapena timabuledi tatunthu
tinadzifunkhira	tinaiwa mwankhanza kuti tikhale nazo zakuba
tinafukizira	tinapereka nsembe zonunkhira bwino
tinapaza	tinapita pa njira yozungulira, tinapitirira
tinatsotsa	tinakhalirako, kukhala pa malo
tinawapululutsa	tinawaononga kotheratu
tinsangalabwi	timiyala (nthawi zina timiyalato ndi tokongola tokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana tolimba kwambiri)
titsose	tikhaliroko, kukhala pa malo, tipumule
titunsirenit	tifunsirenit
tsango	gulu la zipatso, mabalidwe ake amabala mounjikana pamodzi
tsanya	mtengo wina kapena comera cina
tsasa	msasa kapena misasa, mahema
tseketek	mopanda bvuto, mwaubwino
tsinde	munsi mwa mtengo
tumimu	cinthu cimene mkulu wa ansembe wacyuda anasewenzetsa pofunitsa cifuniro ca Mulungu
tyatyatya	pamwamba pa nthaka, kukonza kwa nthaka



thundu

U

ubwadamuke	uphike
ubwatama	udikira
uchetsa	ubala zipatso, kubala kwa zipatso
ucisi	zodetsa

udio	kuipa, kudetsedwa, kusapembedza Mulungu
udzafunkhidwa	udzaberedwa, udzaonongedwa
udzakulaka	udzakhala wobvuta kwa iwe, udzakupambana
udzalalira	udzacita udani, udzabisala ndi colinga kukacita cinthu coipa, udzaononga
udzawafunkha	udzawaononga
udzombole	uthenulire
uguguda	ucaya kwambiri, ugunda kwambiri pa cifuwa
ukakulakani	ukakupambanani, ukalepheretsa
ukunga	uli monga, ulingana
ula	kufufuza za umoyo mwacitsanzo mwa kupita ku ng'anga kapena anthu a mizimu yoipa
ulikubvimvinizika	ulikubvutika, uli kunyoweka, uli kuponderezedwa
uloce	useme
umafunkha	umaba, umaiwa mwankhanza kapena moopseza, umaononga
una	polowera pa dzenje lakhumbidwa kwakuya, citsime
unabuka	unaoneka, unaonetsedwa
unaciwinda	unacilumbira
unakunkhulira-kunkhulira	unakunkhuluka-kunkhuluka
unyenzi	kucoka mobvuta
urimu	cinthu cimene mkulu wa ansembe wacyuda anasewenzetsa pofunitsa cifuniro ca Mulungu
usacibukitse	usacifalitse
usadonthetsa	usaturutse mau, usakambe mau
usakunkhulire	usakunkhuluke
usakwirire	usabise, usabvindikire
usakwiririke	usaphimbike koma ukhale pamtetete
usamadzombola	usamathenulira
usapunamitsa	usatseke pakamwa pa ng'ombe
usapunamiza	usatseke pakamwa pa ng'ombe
usaseama	usakhale pansu mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
usonthokera	uthetsedwa, utengedwa
usonthokeranji	utengedwa bwanji
utawinda	utalumbira
utsotse	ukhalireko, kukhala pa malo, upumule
uwakwirire	uwabise, uwabvindikire
uwapote	uwaphatikize, uwaluke, uwalumikize
uwasule	uwapange kucokera ku cidutswa cimodzi
uzifukiza	uzipereka nsembe zonunkhira bwino

V



vinyo	cakumwa cimene anali kukonze kucokera ku zipatso cimene cisiyana ndi vinyo kapena mowa umene uliko masiku ano
-------	---

W

waarimoni	mtengo wina wace onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wabafuta	wopangidwa ndi nsalu yofewa ya waiti
wabwemba	mtengo wina wace onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wacitando	waukulu m'ufupi mwake
wagudugudu	mtengo umene uli girini komanso uli ndi mayani ambiri
wagugitsa	wafoketsa, waononga, waipitsa
wakasiya	mtengo wina wace onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wakatungurume	wamtundu wina wa cipatso monga kashonati

	onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wakhulungira	adwala kotero kuti afunika pabedi
wakhwimbi	tirigu wokolola
wakubukitsa	wakufalitsa, wofalitsa
wakufunkha	wakuba, munthu woiwa mwankhanza kapena moopseza, munthu woononga
wakulaka	wakupambana, wakugonjetsa
wakulakika	wopambana, wogonjetsa
wakunga	wolingana, uli monga
wakuseama	wokhala pansi mogona cam'mbali pokudya monga mwa cizolowezi ca Ayuda
wakusula	munthu wopanga cinthu kucokera ku cinthu cina
wakutsimphinyo	woyenda cociriwa
wakuwalaka	wobvuta, waukulu, wopambana
wakuwinda	wakulumbira
walakika	wapambana
walinga	wacipupa, wampanda, wamalo otetezeka
wamaluli	waluso
wamangawa	wangongole
wamankhaka	munda wa makiyukamba onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wambanda	cigawenga, woononga, wakupha, wacifwamba
wambawa	mtundu wina wake wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wamkungudza	wamtengo wa mtundu wina umene uli waukulu ndi wolimba komanso womwe umakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wamkuwa	wa mwala wa kopa
wamlombwa	wa mtundu wina wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wam'nsinga	wam'ndende, wotengedwa kapolo
wamphumphu	wanthunthu
wampwamphwa	wolingana mu ufupi mwake ndi mu utali mwake
wamsondodzi	wamtengo womwe umamera m'mbali mwa mitsinje onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wanaphini	wa mtundu wina wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wandipululutsa	wandiononga kotheratu
wangana	wakuti-wakuti, uje
wanjale	mtundu wina wa mitengo
wansangalabwe	wamwala (nthawi zina mwalawo ndi wokongola wokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana wolimba kwambiri)
wansenga	wabwino, votikama
wanhetemya	wodziwa kuimba bwino
wanyonga	munthu woonetsa ulemu ku maganizo a anthu ena, wokhuzidwa msanga
waphanthiphanthi	cidutsa cosalala komanso coonda ca golide
wasafiro	wamwala wa mtengo wapatali
wasitimu	mtengo wina wace onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
wasohamu	wamwala wamtengo wapatali
wathundu	mtengo wolimba wokhala ndi moyo wautali onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi w.
watsanya	wamtengo wina kapena wacomera cina
windani	lumbirani
wobvimvinizika	wonyoweka, wobvutika
wodololoka	wobvutika kwambiri kotero kuti alibe ciyembekezo
wofukiza	wopereka nsembe zonunkhira
wofulika	woduka kapena wocotsedwa ziwalo zobisika za azimuna
wofumuka	woopa, wonjenjemera

wofunkha	munthu wakuba, munthu woiwa mwankhanza kapena moopseza, munthu woononga
wokwiriridwa	wophimbidwa, wobvindikiridwa
wolakika	wopambana, wogonjetsa
wolalira	wocita udani, wobisala ndi colinga kukacita munthu wina coipa
wolama	wabwino, wathanzi
wolamba	wokakamizidwa kutumikira kapena kugwira nchito monga kapolo
wolenda	uta woipa, uta wodonsa, uta wopindika
wolilaka	wolipambana, woligonjetsa
wolipsa	wobwezera
woloca	wosema
wolocedwa	wosemedwa
wololopoka	wofatsa
woluluka	wosalemekezeka, waumphawi, wosawerengedwa
wolunda	wokwiya kwambiri
wooloka	munthu wokhala patali ndi anthu ena cifukwa ca kukhala wodetsedwa
woombera	munthu woluka kapena kupanga zobvala, wopangidwa kapena wolukidwa, wosoka
wopenduza	munthu wokhala pafupi ndi mizimu yoipa, munthu wamatsenga
wophunza	munthu wongoyamba kumene wosaphunzira mokwanira, munthu wangotembenuka kumene
wopinduka	munthu wamitundu amene adatembenukira kwa cipembezo ca Ciyuda (ca Aisrayeli)
wopulukira	wosadziwa, wosamvera, wolakwa
wosomphoka	wautali
wosula	wopangidwa kucokera ku cidutsa cimodzi, munthu wodziwa kupanga malupanga, munthu wodziwa kupasula cinthu ndi kupanga cinthu cina naco
wosulayo	wogulayo
wosusuka	wosakhutira, wodyerera, wopanda malire
wotsimphina	woyenda cociriwa
wotumbuluka	wooneka wa mtundu wa gireyi cifukwa ca kusoweka magari, wosaoneka bwino
wotyasika	wonyenga, wabodza
wounguruma	wolekeredwa, wokhala pa yekha
woweyeseka	wogwedezeka
wowinda	wolumbira
wowirikiza	kupereka cinthu moonjezera, kucita mopambana, wapamwamba
woyalidwa	wotandazyidwa
woyaruka	munthu wamisala, wosokonezeka
wozokota	wolembe pa mwala mwa kusewenzetsa kusema
wozomola	wong'amba, woononga






walombwa




wabwemba



wamkungudza



wakatungurume






wamankhaka

Y

yaalabastero	yamtundu wina wa mwala
yabafuta	yopangidwa ndi nsalu yofewa ya waiti
yaberulo	ya mwala wa buluu (blue) umene umaoneka monyezimira kwambiri
yabuka	yaoneka, yaonetsedwa, yapezeka
yacheni	yosamva kamodzi, yagonthi
yacimphuli	ya pamalo oonekera kuli aliyense
yacitando	yaikulu, yaikulu m'ufupi mwake
yagweregwere	pilala m'mene mulibe kanthu m'kati koma yomangidwa kapena yosemedwa
yakubukitsa	yakufalitsa, yakukulitsa
yakupaza	yakupita pa njira yozunguluka
yamalinga	yazipupa, yampanda, yamalo otetezeka
yambawa	mtundu wina wake wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yamcisu	yamitengo yonunkhira bwino yokhala ndi maluwa ang'ono-ang'ono oyera onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yamikungudza	yamitengo ya mtundu wina imene ili yaikulu ndi yolimba komanso imene imakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yamkungudza	yamtengo wa mtundu wina umene uli waukulu ndi wolimba komanso womwe umakula kwa zaka zambiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yamkuwa	ya mwala wa kopa
yamlombwa	ya mtundu wa mitengo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yamphoyo	ya nyama zina onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yamtanthanyerere	mitengo ina yonunkhira bwino
yamyundo	mvula yoyamba
yancinci	yonyogodola, yomvetsa cisoni
yanjeresi	ya cinthu copangidwa mwa kutentha miyala ina yapadera ndipo cinthu co cinasewenzetsedwa monga pulasta
yankhanambo	ya zilonda, ya khungu loonongeka
yansangalabwe	yamwala (nthawi zina mwalawo ndi wokongola wokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana wolimba kwambiri)
yanthamza	yamitengo ina yake yogwiritsidwa nchito kupanga zobvala onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yasafiri	yamwala wa mtengo wapatali

yasohamu	yamiyala yamtengo yapatali
yathundu	mitengo yolimba yokhala ndi moyo wautali onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi y.
yobwadamuka	yophika
yofukiza	yonunkhira bwino
yofula	yokhala ndi mikwingwirima (zilonda), yoonongeka, yolemala
yokweza	nsembe ina imene inakwezedwa ndi wansembe pamaso pa Mulungu
yoloca	yosemedwa
yondilaka	yondipambana, yondigonjetsa, yondibvuta
yopota	yophatikizana, yolukidwa, yolumikizidwa
yopsapsala	zidutsa za nyama koma za cinyama cacikulu ca m'nyanja (ndico livyatanu)
yopsereza	nsembe ina ya nyama yomwe inatenthedwa yonse pa guwa la nsembe
yosadzombola	yosathenulira
yosomphoka	yaitali
yosumbudzuka	matenda amtundu wina amene amaonetsa tumadontho-madontho tumene tumakhala ku zipupa kwa nyumba
yotanthali	mapulanga yoikidwa pamwamba
yotapira	kutengedwa kwa malo kupatsa mapfuko kapena mitundu
yotsimphina	yoyenda cociriwa
yotyasika	yonyenga, yabodza
yoweyula	nsembe ina imene inanyamulidwa ndi wansembe m'manja ndipo wansembeyo anaiyendetsa uku ndi uku kuionetsa pamaso a Yehova
yoyangayanga	yokula mokumbatirana
yozereweredwa	yokonzeka kucita cinthu, yofuna



Z

zabafuta	zopangidwa ndi nsalu yofewa ya waiti
zacibakuwa	nsalu za mtengo wapatali za mtundu wa pepo
zacitando	zazikulu m'ufupi, zazikulu


zakufunkhidwa	zoberedwa mwankhanza, zakuba
zakukha	zaturutsa
zamalimwe	za m'nyengo yotentha
zamase	cakudya cofewa copangidwa kucokera ku mkaka (chizi)
zamipyololo	za makhala osiyana-siyana (yamizere-mizere)
zamkuwa	za mwala wa kopa
zamphumphu	zanthunthu
zamphwamphwa	zolingana mu ufupi mwake ndi mu utali mwake
zana	hundredi (100)
zansangalabwi	zamiyala (nthawi zina miyalayo ndi yokongola yokhala ndi maonekedwe osiyanasiyana yolimba kwambiri)
zaphanthiphanthi	zidutswa zosalala komanso zoonda
zasundwe	za zogonera kapena zokolola za caka catha
zatumbuluka	zaoneka za mtundu wa gireyi cifukwa ca kusamvera bwino, zaoneka lini bwino
zayalidwa	zatandazyidwa
zenga	jeko
ziboda	zopondera, pansi penipeni pa mapazi a nyama monga ng'ombe kapena bulu
zibuka	zioneka
zibuluma	kukonza nthaka kuti ikhale omasuka
ziciri	citsulo cogwirira cimene tikhomerera pansi
zidikha	malo okhazikika opanda kanthu kena kalikonse onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zidundumwa	zipinda pakati pa khomo lakunja ndi mkatimkati mwa nyumba, mafelemu a makhomo, makhomo
zidzafunkhidwa	zidzaberedwa mwankhanza, zidzaonongedwa kwambiri
zifunkhidwa	ziberedwa mwankhanza
zifunkhidwe	ziberedwe mwankhanza
zigoloondo	njira imene ili ndi zisengu-zisengu
zigono	misasa
zigwa	malo okhazikika amene ali pakati pa maphiri onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zikafunkhidwe	zikaberedwe mwankhanza
zikhato	manja, pakati pa dzanja, muyeso wa 7,5 – 8,5 sentimeta kapena 22 – 25 sentimeta
zikunga	ziri monga, zolingana
zikwi	masauzande (1000)
zimbwi	zopfunda, nsalu, mabulangeti
zimlaka	zimpambana, zimgonjetsa
zinabuka	zinaonetsedwa, zinapezeka
zinaguguda	zicita mdidi
zinandilaka	zinandipambana, zinandigonjetsa, zinandibvuta
zinatofa	zinafota
zinatunsidwa	zinacotsedwa
zing'anda	dzanja lonse lioneka monga golide
zinganga	zinthu zazing'ono za neklesi (zobvala m'nkhosi)
zinkhanira	zimphanira onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zinkhoma	mbuzi zokhala ku mapiri ndi zokwera ku maphiri
zinkhwamba	mayani akulu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zinziri	timbalame tating'ono onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
ziputu	maphesi youma, gaga, udzu youma
zisanabuke	zisanaoneke, zisanapezeke
zisingikira	zasungidwira, kusungidwa
zisumbu	malo ozunguliridwa ndi madzi mbali zonse
zitando	misasa (ya nkondo)
zithando	misasa (ya nkondo)

zithuntha	nyama zicinya pobadwa mwana
zitikumike	zitikomane, zitipeze
zitiipula	mibedi, mitundu ina ya kalimidwe
zitsukwa	mcira
zitumbuluka	zioneka za mtundu wa gireyi cifukwa ca kusamvera bwino, zioneka lini bwino
zitunda	mapiri ang'ono
ziunda	malo yapamwamba imene wina aliyense akhoza kukuona
ziundo	polowera, pakhomo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zivi	mwezi wa Ayuda uli pakati pa April mpaka pakati pa May
ziwalamsatsi	mtundu wina wa dzombe
ziyalika	zitandazya
ziyangayanga	zikula mokumbatirana
zobuka	zioneka, zoonetsedwa, zapezeka
zobvimvinika	zonyoweka
zofukiza	zonunkhira bwino poperekedwa monga nsembe m'cipembedzo
zofula	zocepa zaka, tung'ombe twatung'ono
zofunkha	zakuba
zokundika	zosonkhanidwa, zounjikidwa, katundu
zokweza	nsembe zina zimene zinakwezedwa ndi wansembe pamaso pa Mulungu
zolakika	zopambana
zolenjeka	nsalu zina za zolukidwa
zolulutsa	zonyoza, kudzikiza
zombo	zibwato zazikulu onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zondikungudza	zazikulu, zondiononga
zonika	zopenta, zopentedwa
zopota	zophatikizana, zolukidwa, zolumikizidwa
zopsereza	nsembe zina za nyama zomwe zinatenthedwa zonse pa guwa la nsembe
zopsyerera	zoonongedwa ndi mphepo
zopululutsa	zionongeko
zothonana	mtengo umene uli ndi mayani ambiri
zothwikira	zida zakuthwa cimene bulu kapena ng'ombe sakhoza kuponya kwendo yake kumboyo onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi z.
zotsetseremba	zinthu zina zooneka monga makorona
zotsimphina	zoyenda cociriwa
zotumbuluka	zooneka za mtundu wa gireyi cifukwa ca kusamvera bwino, zosaoneka bwino
zoundukula	zipatso zoyamba za zokolola
zowawanya	zakuba, zoononga
zoweyula	nsembe zina zimene zinanyamulidwa ndi wansembe m'manja ndipo wansembeyo anaiyendetsa uku ndi uku kuionetsa pamaso a Yehova
zowinda	malumbiro
zowirikiza	kupereka zinthu moonjezera, kucita mopambana, kupereka zinthuzo moonjezera m'mene iwe unacitira
zoyangayanga	zokula mokumbatirana
zozerewera	zokonzeka kucita cinthu, zofuna
zozokota	zolemba pa mwala mwa kusewenzetsa kusema
zunguniza	zungulira







zinziri




zidikha



zothwikira



zinkhwamba



zigwa

Kodi ico ndi ciani?

Buku ili ndi la aliyense okonda kuphunzira za m'Baibulo.
M'bukuli mupeza mau ofanana ndi mau osadziwika a m'Baibulo la m'Chichewa.

Malangizo ogwiritsira nchito bukuli

1. Werengani Baibulo tsiku ndi tsiku. Mukakomana ndi liu losadziwika, tengani bukuli.
2. Yang'anirani cilembo coyamba ca liu lomwe mufuna kudziwa liu lofanana nalo.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula*, cilembo ico ciyamba ndi *a*.
3. Pitani patsamba lomwe cilemboci calembedwa ndi cilembo cacikulu.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula* muyenera kupita pa tsamba lomwe A yalembedwa ndi cilembo cacikulu (tsamba 2).
4. Yang'anani cilembo caciwiri ca liu lomwe mufuna kudziwa liu lofanana nalo. Kenaka pitani pansi pamndandanda mpaka mutafika pa mau okhala ndi cilembo coyamba ndi caciwiri comwe mufuna.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula* mupite pansi pamndandanda mpaka mutafika pa mau oyambira ndi *a-n*.
5. Citani cimodzimodzi ndi cilembo cacitatu, cacinai ndi zina za liu lanu mpaka mutapeza liu lomwe mufuna kudziwa.
Mwacitsanzo, ngati mufuna kudziwa za liu lokamba kuti *anangula*, londolani mndandanda a-n-a-n-g-u-l-a ndipo mudzaona kuti liuli ndi lopezeka pa tsamba 4.
6. Ngati liu limene mwapeza afunika cithunzi-thunzi, pezani cithunzi-thunzi ico pothera pa mau.
Mwacitsanzo, pansi pa liu lokamba kuti *anangula* ndi lolembedwa *onani cithunzi-thunzi pothera pa mau oyambira ndi a*. Mudzapeza cithunzi-thunzi ca *anangula* pa tsamba 6.



Civumbulutso 1.3: Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene akumva mau a cineneroco, nasunga zolembedwa momwemo; pakuti nthawi yayandikira.